# Baibulo ya ana

Ikupasilani



# Lonjezo la Mulungu Kwa Abrahamu

Yolembedwa ndi: Edward Hughes
Yojambulidwa ndi: Byron Unger; Lazarus
Alastair Paterson
Yotengedwa ndi: M. Maillot; Tammy S.
Yotathauzidwa ndi: Mphatso Amiel
Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

BFC
PO Box 3
Winnipeg, MB R3C 2G1
Canada

©2020 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.





Patapita nthawi chitatha chigumula, anthu anapanga ganizo.


"Tidzamanga mzinda waukulu wokhala ndi nsanja imene ikafika kumwamba," anatero. "Tizikhala pamodzi nthawi zonse." Wina aliyense amalankhula chilankhulo chimodzi.
3


Mulungu amafuna kuti anthu azikhala paliponse pa dziko limene analenga. Anapanga chinthu chofunikira. Nthawi yomweyo magulu a anthu anayamba kulankhula mosiyana. Mulungu anawapatsa zilankhulo zatsopano.
4


Amene amalankhula chilankhulo chimodzi anachokera limodzi. Mwina amapanga mantha ndi anzawo kuti sazimvana.
5


Munjira imeneyi, Mulungu anapangitsitsa anthu kuti akhale mmayiko osiyanasiyana. Mzinda umene anausiya unkatchedwa Babelo kutanthauza kuti Chisokonezo.
6


Patapita zaka zingapo, kumalo otchedwa Uri waku chaldees, Mulungu analankhula kwa munthu wotchedwa Abramu. "Choka kuno," Mulungu analamula. "Pita kudziko limene ine ndidzakulozera."
7


Abramu anamvera. Mulungu anamutsogolera ku Kanani. Mkazi wake Sarai ndi Mphwake Loti anapitira limodzi.
8


Ku Kanani, onse Abramu ndi Loti analemera. Anali ndi ng'ombe zambiri. Kunalibe chakudya chokwanira cha ziweto zambiri.
9


Abusa a Loti anakangana ndi abusa a Abramu. Abramu anati, "pasakhale vuto, tidzasiyana, Loti tenga mbali ya malo amene ukufuna."
10


Loti anasankha mbali yayikulu ya chidikha cha msipu chokhala ndi mizinda ndi midzi patalipatali ndipo kumaoneka bwino. Koma mizinda inali yaumfiti.
11


Atangochoka Loti, Mulungu analankhulanso kwa Abramu. "Ndikupatsa dziko lonse la Kanani ndi ana ako mpaka kale." Abramu ndi Sarai analibe ana. Zingatheke bwanji kuti
Mulungu asunge lonjezo lake lalikulu chonchi.
12


Amuna atatu ochokera kwa Mulungu anadza kwa Abramu ndi Sarai. "Udzakhala ndi mwana wamamuna posachedwa," anatero. Sarai anaseka. Sanakhulupirire uthenga wa Mulungu.
13


Anali ndi zaka makumi asanu ndi anayi. Mulungu anamuuza Abramu kuti adzatchedwa tsopano Abrahamu {Bambo wa Fuko} ndipo Sarai adzakhala Sara {Mkazi wa Mfumu}.
14


Mulungu anauzanso Abrahamu adzaononga mizinda iwiri yonyasa ya Sodomu ndi Gomora. Mphwake wa Abrahamu Loti anali kukhala ku Sodomu pamodzi ndi mkazi wake.
15
Loti anakhulupirira pamene chenjezo la Mulungu linabwera, koma amuna a ana ake akazi anakana kuchoka ku Sodomu. Zinali zoopsya bwanji! Sankakhulupirira mawu a Mulungu.
16
Loti yekha pamodzi ndi ana ake akazi awiri ndiwo anapulumuka. Moto wang'anjo unagwera mzinda wotembereredwawo.
17
Zokhumudwitsa, Mkazi wa Loti sanamvere chenjezo la Mulungu ndipo anacheuka m'mbuyo pamene amathawa. Anasanduka mwala wa mchere.
18
Ambuye anasungabe lonjezo kwa Abrahamu ndi Sara. Ndipo anakhala ndi mwana muukalamba wao monga Mulungu ananenera. Anasangalala bwanji atamuona Isake atabadwa!
19
Mwina Abrahamu ankaganiza kuti lonjezo la Mulungu lompatsa iye pamodzi ndi ana ake dziko la Kanani lidzakhala lakale.
20

Mulungu adzasunganso lonjezanolo. Mulungu amasunga malonjezano ake nthawi zones.





Lonjezo la Mulungu Kwa Abrahamu

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

Genesis 11 - 21

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130



# Mapeto

4 60



Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16